# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2025-2026 M'BOMA LA BALAKA

## Dzinja la 2025/2026 Mwachidule

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.


Boma la Balaka likuyembekeza kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena wocheperapo mu nyengo ya dzinja ya 2025/2026.

## October 2025




Madera ambiri kudzakhala kopanda mvula mu mweziwu. Koma pali kuthekera kodzakhala ndi mvula ya Chizimalupsya m'madera ena yosaposera 30mm, yomwe idzakhale ya mphepo ya mkuntho ndi mphezi.


## November 2025




Tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepera apo mu mweziwu.

Madera ambiri akhoza kudzalandira mvula ya mlingo wa pafupifupi 50mm yomwe idzakhale ya mphepo ya mkuntho komanso mphezi.


## December 2025




Mu mwezi wa December madera ambiri akuyembekezera kuzalandira mvula yamulingo okwana 150 mm. Komabe, madera ena a kumzambwe kwa kwa T/A Kalembo ndi kumpoto kwa Balaka Boma akuyembekezeka kuzalandira mvula yokwana 250–300 mm.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuzagwa kuyambira sabata lachiwiri la mwezi wa December 2025.


## January 2026




Mwezi wa January ukuyembekezeka kukhala wa chinyontho. Madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo okwana 250mm ndi ena ochepa kulandira mvula ya mlingo osaposera 200mm monga ngat madera a kwa T/A Nsamala, T/A Kalembo ndi Balaka Boma.

Ng'amba yosabzola sabata limodzi ikuyembekezeka mu m'mweziwu.


## February 2026




Mvula yokhazikika kapena kuchepera apo ikuyembekezeka kufika mlingo okwana 150mm mpaka 200 mm. Madela ena mu Balaka Boma akuyembekezera kuzalandira mvula yapafupifupi 250mm.

Ng'amba yosabzola masabata awiri ikuyembekezeka mu mweziwu.


## March 2026




Mvula yokhazikika kapena kuposera apo ikuyembekezeka kuzagwa ndi mlingo okwanira 100 to 150 mm mu mwezi umenewu.

Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lomaliza la mwezi wa March 2026.

## April 2026





Madera ambiri akuyembekezera kuzalandira mvula yamlingo okwana 0mm mpaka 30 mm pamene nyengo yamvula ikupita kumapeto.

Boma la Balaka likuyembekeza kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena wocheperapo mu nyengo ya dzinja la 2025/2026. Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuzagwa kuyambira sabata lachiwiri la mwezi wa December 2025. Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lomaliza la mwezi wa March 2026. Ng'amba yosapzola sabata imodzi ikuyembekezeka mu mwezi wa January, ndipo yosapzola masabata awiri ikuyembekezeka mu mwezi wa February. Nyengo yonse ya dzinja ikuyembekezeka kukhala ya masiku apakati pa 110 ndi 120.

Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.

| BALAKA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 9.8 | 44.6 | 15.7 |
| NOV | 66.6 | 123.2 | 66.8 |
| DEC | 182.7 | 319.5 | 190.0 |
| JAN | 270.9 | 432.1 | 265.4 |
| FEB | 163.6 | 252.1 | 225.8 |
| MAR | 127.6 | 199.3 | 115.5 |
| APR | 10.8 | 59.2 | 33.2 |





**Ulosiwu udzaunikidwanso mu mwezi wa December 2025**
For further information contact: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808, Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zapangidwa ndi kusindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: